

Danieli : 7:7-13

Mutu : Nyangayaying'ono ndi mwana wamunthu

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Tiyeni lero Ambuye atitsogolere ndi mau ake apa Luka 10:20, amene akuti, “Koma musakondwera nako kuti mizimu idakugonjerani, koma kondwerani kuti mayina anu alembedwa m’Mwamba.”

Tsono mupologalamu yatha tinali kusanthula Danieli 7:1-6, momwe timapitiliza kuona masomphenya a Danieli a zirombo zinayi. Ndipo lero pa Danieli 7:7-13, tikambirana nkhani ya nyangayaying'ono ndi mwana wamunthu.

7. Pambuyo pake ndinaona m’masomphenya a usiku ndi kuona chirombochachinayi, choopsa ndi chochititsa mantha, ndi champhamvuchoposa, chinali nawo mano akuru achitsulo, chinalusa ndi kuphwanya ndi kuponderezachotsala ndi mapazi ake; chinasiyana ndi zirombo zonse zidachitsogolera; ndipo chinali ndi nyanga khumi.

Mugawo lino, Danieli akuika maso ake pa chirombochachinayi. Komanso tiyenera kudziwa kuti ulosi nthawi yonse umafotokonza za m'tsogolo kupyola zinthu zomwe zachitika kale m'mbuyomo. Ndiye tikunena kuti kudzera m'chirombochachinayichi, tipeza kuti dziko lapansilaonetsa mphamvu yonse yotsutsa Mulungu.

Tsono tikunena kuti chirombo ichi, chosadziwikachi, chikuimira ufumu wa Roma monga muja miyendo ya fano la Nebukadneza linaonetsa. Mu verse 19-28, ndimo tidzapezakufotokonzerakweni-kwenikwa nkhani imeneyi. Ndiye monga ndinanena kale kuti maso athu tsopano ali pa chirombochachinayi, chifukwa ndiyo ndime yofunika kwambiri kwa ife lero lino popeza tikukhala m'masiku a chirombo chimenechi. Iyi, ndi nthawi yomwe zala khumi ndi nyanga khumi zikuyambakuonekera.

Tsono taonani kutichirombochachinayichija, ndichosiyana kwambiri ndi zirombo zina zija. Ndipo chirombo ichi, chaonetsedwapachokha-chokham'masomphenya ake. Nkhani ikunena kuti nyama zinazi, ziri ndi nyama zizakezofanananazokutchire. Inu ndinu mboni kuti mkango,

chimbalangondo ndi nyalugwemuzidziwa, koma sindikhulupirira kuti mudayambamwaonanyama yachinayi pansi pano, m'madzi ngakhale mumlengalenga. Ichi, ndichirombochachilendo, kotero kuti inu mutachionasindikhulupirira kuti mukhoza kupeza turo ayi. Nyama iyi, ndiyaukari, yopsa ndi yamphamvu zochuluka. Kutsindika kunena kuti nyama imeneyi ilibeinzake, kotero kuti inu mukhoza kuizindikira chifukwa cha mphamvu zake, kuopsa kwake pakuthyola ndi kuononga nyama zinzake.

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani pano tikunena kuti kafotokonzedwe aka kanyama iyi, kakufanana ndi ufumu wachinayi uja mu Danieli 2:40, momwe muli miyendoyachitsulo ndi mapazi a dongo. Taonani miyendoyachitsulo iyi, ndiyo ikufanana ndi mano a chitsulo, amene akugwiritsidwa ntchito pakuphwanya zinthu. Ndiye pamene tinena zanyanga m'mau a Mulungu, tipeza kuti imaimira mphamvu. Tsono taonani kuti chirombochachinayichi, chiri ndi nyanga khumi, kotero kuti mukhoza kuona kuchurukakwa mphamvu ya chirombo chimenechi.

Pamene tiwerenga pa Danieli 2:24, tipeza kuti nyanga khumi izi, zikuimira mafumu kapena ufumu khumi, zomwe zikufanana ndi zala khumi mu fano la Nebukadnezzara. Tsono tikunena kuti kuonetsedwakwanyanga khumi pamutu pake zikuonetsa kukhazikika ndi kukwanira ponse-ponse kwa ufumu wamphamvu. Kutanthauza kuti ufumu wa Aroma, ndiwo ufumu womwe poyamba unafungatiramayiko khumi a Italy, France, Spain, Germany, Britain, Sarmatia, Pannonia, Asia, Greece ndi Aigupto. Tsono ngakhale ufumu uwu unatha, koma udzakhala nthawi yaitari chifukwa udzasonkhanitsidwansokufikira kukhazikitsidwa kwa ufumu wa Mesiya.

Masomphenya a chirombochachinayichi, ndiwo ofunika kwambiri kwa inu ndi ine, popeza asanakwaniritsidwe kufikira mtsogolomo. Koma tiyenera kudziwa kuti tikukhala m'masiku, amene akuyandikira ku nthawi yachimaliziro ya pansi pano. Tikunena kuti ufumu wa Aroma unakhazikitsidwa kale ndipo unatha, koma udzabwereransoku mafumu khumi, momwe udzakhazikitsidwanso ndi wotsutsa Kristu.

8. Ndinalikulingirira za nyangazi, taonani, pakati pa izo panaphukanyanga yina, ndiyo yaing'ono; patsogolo pake zitatu za nyangazoyambazizinazulidwa ndi mizu yomwe ndipo taonani, m'nyanga m'menemo munali maso ngati maso a munthu ndi pakamwa palikunena zazikuru.

Tsopano ndifuna tiike maso athu pa nyanga khumi, koma sizikutanthauza kuti panali ufumu wachisanu ayi. Izi, ndinyanga zomwe zidamera pamutu pa chirombochachinayi chija. Ndiye mu masomphenya oyamba, tidaona fano lomwe linali ndi miyendoyachitsulo ndi mapazi a dongo. Chitsulo ichi, chikanalipo chomwe ndi Roma, koma dongo kapena dothi, likuimirakufookakwa ufumuwu. Mwanjira ina tikunena kuti chitsulo chikuimira ulamuliro wamphamvu wa munthu m'modzi (autocratic), pamene dongolikuimira ulamuliro wagulu, wofooka wa (democracy).

Tsono ndikoyenera kunena za kufookakwa ulamuliro wa democracy. Inu ndi ine, lero lino ndife wonyadira chifukwa cha ulamuliro wa democracy. Apa, tiyenera kuyamika Mulungu chifukwa cha ulamuliro umenewu, koma tikaonetsetsa ulamuliro uwu, uli ndizofoka zake. Chofoka chachikulu ndi chakuti inu ndi

ine, ndife anthu ofunika pamasankho pokha, koma pakupangaziganizo inu, ndi ine, sitikhala anthu ofunika ayi. Tikunena kuti anthu andale panthawi yamasankho amanena kuti inu ndi ine, ndife ofunika popeza ndife eni ufulu. Koma tikafika pankhani yaulamulirowadziko, ifetiribe mphamvu. Taonani kuti anthu andale ndi iwo a mabungwe ndiwo amene akulamulira dzikoli pakupanga zomwe afuna. Tikunena kuti ndizabwino ndithu kukhala ndi ufulu wa democracy, koma sitili paufulu pakuyendetsaboma.

Ndiye ndifuna muone kuti Boma la Mulungu sila democracy ayi. Ili, ndilo la ulamuliro wa dictatorship, ulamuliro wa m'modzi. Ndikunena mau amenewa chifukwa pamene Ambuye Yesu adzakhazikitsa ufumu wake pansi pano, sadzafunsirakwa munthu wina aliyense ayi. Iye, adzachita chomwe Iye afuna kuti chichitike. Kunena kuti Ambuye Yesu ndiwo adzasankha chinthu choyenera kuchitika kotero kuti dzikoli lidzayendetsedwa momwe Iye afuna. Ichi, ndichifukwa chake inu ndi ine, tiyenera kukangamira Kristu, chifukwa ngati inu simuteromudzasowa mtendere ndi ulamuliro wake. Kutsindika kunena kuti Ambuye

Yesu adzachotsa chinthu china chilichonse chosayeneramuufumu wake, komanso anthu onse amene atsutsana naye. Nkhani ikuti inu ndi ine, tiyenera kubvomereza ulamuliro wake, umene ndiwamphamvu, wokwanira komanso wosakaikitsa.

Taonani ufumu wa Roma unasokonekera chifukwa cha mabvuto a mkati mwa ufumuwo monga makhalidwe oipa, a katangale, a chiwerewere ndi uchidakwa. Koma chofoka chachikulu ndi kuti maufumu anayi onsewa anagwa pansi chifukwa cha uchidakwa. Ndiye ndifuna muone kuti m'dziko lathu lino, tikunena kuti mankhwalaozunguza bongo, ndioletsedwa pamene mowandiwbvomerezeka. Kodi apa, tikunyenga ndani? Ichi, ndichifukwa chake munthu wina adalembakabukukakang'ono momwe amayesakuyankha funso lakuti, Kodi chidakwachingakweze dziko? Nkhani ikunena kuti alipo anthu ambiri amene alim'maudindoapamwambam'boma komanso m'mabungwe. Kodi ndichithunzi ichi, mukukhulupirira kuti dziko lathu likhozakutukuka? Yankho likuti ndikosatheka kuti dziko likhoza kupita patsogolo. Ndikunena zimenezi chifukwa

mum'chitidwewoledzera ndimo mungaka yake yazikonzero zoipa monga; kuba, kupha, dama, kadukandi zonyasa ziri zonse.

Tsono pamene tikamba nkhani ya nyangayaing'ono, tikunena kuti ndiyo nyanga yomwe inaonekayaing'ono, koma pambuyo pake, inaoneka yaikulu koposa zonse. Kunena kuti ufumu wa Roma sudapitilire ndi Alexander, koma ulamuliro wa German, umene unali kutchedwa ufumu woyera wa Aroma. Izi, zinali chimodzimodzi ndi ufumu waNapoleon ndi Kaisara, kuti ufumu wawo, unali ufumu wa Aroma. Kutanthauza kuti ufumu wa Aroma ndiwo ufumu wa dziko lonse ngakhale kuti unalephera m'mbuyomo, kutsimikiza kuti chitsulo sichinagwirane ndi dongo.

Koma taonani kuti nyangayaing'onoidza ikuonetsa kuti mphamvu ina yotsutsa Mulungu ikuphukiram'maufumu omwewo. Uyu, ndiye munthu wochimwa, amene akumutchula Paulo pa 2 Atesalonika 2:3, kuti, "Munthu asakunyengenikonseko; kuti silifika, koma chiyambechifikechipatukocho, nabvumbulutsike munthu wosayeruzika, mwana wa chionongeko." Tamvani 1 Yohane 2:18, akunena kuti, "Ana inu, ndi nthawi yotsiriza iyi; ndipo monga mudamva kuti wokana kristu akudza, ngakhale tsopano alipo

okana Kristu ambiri; mwa ichi tizindikira kuti ndi nthawi yotsiriza iyi.”Ndipo pa verse 22, pali mau akuti, “Wabodzandani, koma iye wokanayo kuti Yesu siali Kristu? Iye ndiye wokana Kristu, amene akana Atate ndi Mwana.”Nkhani yonseziikungoonetsa kulowa ndi kukhazikikakwa m’chitidwe woipa, womwe unayambika komanso kugwa kwa ufumu wa Roma. Kutanthauza kuti nyangayaing’ono ikuimira wokana /wotsutsa Kristu, amene akudza pambuyo, pamene Kristu asanadze kachiwiri.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna kunenetsa kuti malinga ndimomwe tasanthulira maufumu ochulukawa, ndiye tikupeza kuti ufumu wa Papa ku Roma ndiwo umene ukugwirizana kwambiri ndi wokana Kristu, popeza ndiye amene amanena kuti ali ndi mphamvu za Mulungu padziko lonse pansi pano. Kutanthauza kuti ndiye akulamulira m’malo mwa Mulungu, momwe akuonetsa Mzimu wokana Kristu chifukwa cha mau apaMateyu 28:18, Ambuye Yesu akunena kuti, “Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi.”

Komanso taonani kuti chirombo ichi, chiri ndi maso amene akunga a munthu. Kutanthauza kuti chirombo ichi, ndi munthu amene

akutchula kuti ndi wopembedza, pamene ali wokana Kristu. Izi, zimachitika mwa nzeru ndi mochenjerapopeza ndiwooneka bwino ndiwosakaikidwa, koma ali ndi cholinga chofuna kupeza mphamvu ndi ulamuliro pakayendetsedwekadziko ndi chipembedzo. Tere, ndichifukwa chake pakamwa pake pamaturuka mau akuti, ndiye wolowa m'malo mwa Petro, mutu wa mpingo, amene ali ndi mphamvu m'mwamba, padziko lapansi ndi kugahena komwe, kotero kuti akhoza kukhululukira machimo, kumvera chisoni wolakwa, kupanga malamulo atsopano komanso ngakhale kuchotsa malamulo ena a Mulungu. Tsono pazonsezi mau a Mulungu pa Chibvumbulutso 13:5, akuti, "Ndipo anachipatsa m'kamwa molankhula zazikuru ndi zamwano; ndipo anachipatsa ulamuliro wa kutero miyezi makumi anayi ndi awiri."Kutanthauza kuti chithunzi cha chirombo ichi, chokhala ndi maso ndi pakamwa chikuonetsa kuti ndiye munthu, amene akhoza kulankhula zinthu zazikulumodzikweza ndi mochitira Mulungu mwano.Tsono mwa malankhulidwe a mwano, wodzikweza ndizo zikuonetsa Mzimu woukira Mulungu. Tere izi, ndizo zimene wokhulupirira ayenera kuyembekeza kuti zidzakwanitsidwa posachedwa monga mwa mau apa Danieli 7:25, amene akuti, "Ndinena mau akutsutsana ndi

Wam'mwambamwamba, nidzalemetsaopatulika a
Wam'mwambamwaba, nidzayesa kusintha nthawizo ndi chilamulo;
ndipo adzaperekedwa m'dzanja lake mpaka nthawi imodzi ndi
nthawi zina ndi nthawiyanusu.”

9. Ndinapenysera mpaka anaikapomipando yachifumu,
 nikhalaponkhalamba ya kale lomwe, zobvala zake zinali za
 mbuu ngati chipalechofewa, ndi tsitsi la pa mutu pake ngati
 ubweya woyera, mpando wachifumu unali malawiamoto, ndi
 njinga zake moto woyaka.”

Nkhani pano yasintha kotero kuti tsopano tiona nkhani ya
Kumwamba, ndipo chithunzi chomwechikuonetsedwa pano ndi cha
mpando wachifumu wa Mulungu. Ichi, ndicho chithunzi chomwe
chikuonetsedwanso pa Chibvumbulutso 4 ndi 5, nkhani
yokonzekera chilango cha chibvuto chachikuru ndi kubwera
kwachiwiri panso pano kwa Ambuye wathu Yesu Kristu.

Ndiye tamvani, pamene akunena kuti, “Ndinapenysera...”,
akutanthauza kuti Danieli anali kuonabe zinthu zachilendo
zimenezi ndi kumaganizira kuti zitanthauza chiyani. Tsono
popitanthawi Danieli anaona muulemererowa Mulungu, chilango

chikuperekedwa pa chirombochachinayi chija ndi kuchotsa mphamvu ndi kudzikweza konse kwa chirombocho. Ndiye zochitika zonsezi, zikungoonetsa kuti ndizo zikonzekero za ulamuliro wa woyera mtima pansi pano. Kutanthauzo kuti woyera mtima adzatumikira Ambuye wathu Yesu Kristu muufumu wake pansi pano.

Wokondedwa anzanga apaulendo, pamene tinena kuti chilango chidzaperekedwakwa wokana Kristu, tikutanthauza kuti Mulungu ndiye oweruza wolungama. Kutsimikiza kuti anthu onse woipa pamodzi ndi iwo wochita chinyengo m'chipembedzo chawo, adzalandira chilango ndithu. Tamvani mau apa Masalmo 37:13, akunena kuti, “Ambuye adzamseka: popeza apenya kuti tsiku lake likudza.”

Ichi, ndichifukwa chake Danieli akuona kuti ufumu wonseudzathapamodzi ndi mau onse aulamuliroamene atsutsana ndi ufumu waMulungu. Paulo anatsimikiza mau amenewa pa 1 Akorinto 15:24, pamene anati, “Pomwepo pali chimariziro, pamene adzapereka ufumu kwa Mulungu, ndiye Atate, atathakuthera chiweruzo chonse ndi ulamuliro wonse ndi mphamvu yomwe.”

Tsono ubweya woyera, mpando wachifumu unali ndi malawiamoto...” ukuimirakulungama kwa woweruza, amene akudza kudzapereka chilango kwa wokana Kristu. Uyu, ndiyemweakufotokonzedwa pa Chibvumbulutso 1:14, pamene akuti, “Ndipo tsitsi la pamutu pake linali loyera ngati ubweya woyera, ngati chipalechofewa; ndi maso ake ngati lawi la moto.”

Koma muyenera kudziwa kuti ichi, sichiweruzochotsiriza ayi, popeza nthawi yachiweruzochotsiriza sikudzakhala dziko lapansi ngakhale zonse tikuziona m’dziko lino. Izi, zidzachitika mu ufumu wa Kristu pano pansi umene udzakhala kwa zaka chikwi, umene udzasinthana ndi ufumu wa Mulungu wamuyaya. Iyi, ndiyo nkhani ili pa Chibvumbulutso 11:15, imene ikuti, “Ndipo mngelo wachisanu ndi chiwiri anaomba, ndipo panakhala mau akuru m’Mwamba ndi kunena Ufumu wa dziko lapansi wayamba kukhala wa Ambuye wathu ndi wa Kristu wake: ndipo adzachita ufumu kufikira nthawi za nthawi.”

10. Mtsinje wamotounayendawoturuka pamaso pake, zikwi zikwianamtumikira, ndi unyinjiwosawerengekaunaima

pamaso pake, woweruza mlandu anakhalapo ndi mabuku
anatsegulidwa.

Tsono ichi, sichithunzichachiweruzo chachikulu pampando woyera
wa Mulungu ayi, koma zinthu zonsezizikungoonetsakutha kwa
ulamuliro wa wokana Kristu pansi pano, nthawi yomweyo ufumu
wa Kristu udzakhazikitsidwa. Kutsimikiza kuti dzikoli lidzalandira
chiweruzo popeza likuyenda mumdima. Kutsindika kuti wokana
Kristu ndiye amene akupereka ulemerero wamba, umene uli
ulemerero wopanda mtanda.

Tsono mu verse 11-12, tiona chithunzi chakuti pamene Mulungu
akukonzekera za chiweruzo m'Mwamba, ndipo pamene wokana
Kristu adzadzikweza kopambana komanso padzakhala chimaliziro
cha ufumu wake. Ndiye tiyenera kudziwa kuti ngakhale maufumu
atatu aja anatha kale, koma udzakhale ukuonetsa kuzunza
kwake m'nthawi ya Chibvuto chachikuru.

13. Ndinaona m'amasomphenya a usiku, taonani anadza ndi
mitambo ya Kumwamba wina ngati mwana wa munthu,
nafika kwa nkhalamba ya kale lomwe; ndipo
anamyandikizitsa pamaso pake.

Tsono Danieli sakuona zizindikiro monga za nyama zija ayi, koma akuona kukhazikitsidwa kwa ufumu wa Mesiya ndi woyera mtima wonse. Ndipo Danieli akuti anaona mwana wa munthu, dzina lomwe m'Chipangano Chatsopano, Ambuye Yesu akudzitanira. Uwu, ndiwo udindo womwe Mesiya adzagwiritsa ntchito poonongachirombochachinayinalandira mphamvu ndi ulamuliro wa Iye mwini, mwakupatsidwa ndi Atate wake kukhala Mfumu ya mafumu onse.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tiyeni titsirize ndi mau akuti, Ambuye wathu Yesu Kristu ndiye mwalawosemedwa wopanda manja, umene udzathyola fano, nadzakhazikitsa ufumu wake pansipano. Kutsimikiza mau apa Masalmo 2:9, akuti, “Udzawathyola ndi ndodo yachitsulo; udzawaphwanya monga mbiya ya woumba.” Kutsindika kuti pamene Mesiya akubwera kachiwiri, ufumu wa satana, udzathyokapamodzi ndi onse womuukira Iye ndipo onse womvera Iye, adzalowa mu Ufumu wake. Kodi inu mwakonzekera kulowa mu Ufumu umenewu?

Kwalerotilekeza pano.Ndipo tinali kusanthula Danieli 7:7-13,
momwe timakambirana nkhani ya nyangayaying'ono ndi mwana
wamunthu.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!